


MWINJIRO WOSIYIRIDWA

 Ine ndinali mkati ndi abusa. Ine ndinati...Ine ndinawapempha iwo dzulo kuti andiyimbire foni. Ndipo ine ndinadzapeza, ine basi...Tsiku lonse, panalibe mafoni, ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ndikudabwa ndi chiyani chavuta? Chinachake ndi...Chirichonse chiri mwamtendere.” Ndipo patapita kanthawi, Mlongo Wood anabwera ndi mafoni ochuluka. Foni yanga inali itazima, chotero, ngati aliynse wa inu munayimba. Foni imalira, koma iyo siimamveka mmenemo, chotero vuto linali pansu koyatsira. Iwo anadzaikonza iyo pafupifupi eyiti koloko usiku wathawu, kapena mwinamwake pang’ono iyo isanakwane, ndipo, foni, mafoni akumabwera tsopano.

² Ndife okondwa kukhala mu msonkhano mmawa uno. Ine ndiri ndi chimfine choyipa, chimene kawirikawiri ndimakhala nacho ndikabwera kwathu. Kuyenda mchিপale mpaka mchiuno mwako, ndi kugona panja usiku. Osaganizira konse za izo kutali ndi kuno, koma kungowoloka phiri limenelo uko ku New Albany, ndizo zonse zimene iwe uyenera kuchita, ndikafika mchigwa chino, ndiye ndimakhala ndi chimfine choyipa. Ndipo ndi a... Ine sindikudziwa, pali chinachake mchigwa muno chimene chimatsitsa icho. Ndipo ndi kotsika, ndipo basi sindigwirizana nako konse.

³ Tsopano, ndife okondwa kukhala pa tchalitchi, monga ndanenera, ndi kumamumva m’busa wathu wokonedwa akupereka mawu ake opempha kwa ife, ndi kwa Ambuye Yesu. Ndi—ndi kumva, zachisoni kumva ambiri akudwala ndi osowa, ndi momwe mdierekezi walusira kumupangitsa aliynse kudwala.

⁴ Ndipo dona wamng’ono anaimirira chifukwa cha mchewali wake kumbuyo uko, ndipo ine ndikumudziwa wa Mlongo Sauer kumusi uko anali ndi iye. Adokotala anamutumiza kunyumba kuti akafe tsopano. Ndipo iye akukhulupirabe kuti iye achira. Ndipo iye ali modwalika, chikhalidwe chodwalika kwambiri. Apongozi anga aakazi, mwanjira yomweyo, usinkhu wa zaka sevente tsopano. Iye ali mu chikhalidwe chovuta kwambiri. Ndipo ndithudi matenda ochuluka kuzungulira kuno. Ndiyeno kuli Mzimu Woyera kozungulira kuno, mwaona, umene umachiza matenda athu, ngati ife tingathe kupeza kukonderedwa ndi Iye.

⁵ Ndipo tsopano, popeza kuti mmero wanga uli ndi zilonda, osati zilonda, koma wasasa. Ndipo ine sindiyesera kuti ndilalikire, koma ndingoyankhula ndi inu kanthawi kuchokera mu Mawu, ndipo kenako tipita mu kupempherera odwala,

chimene ine ndinalonjeza kuti ndidzachita. Koma basi ndisanachite izi, ndikufuna kuti ndilengeze misonkhano ina yowonjezera. Ine . . .

⁶ Mmautumiki anga ine ndakhala ndiri ndi kutsutsa pang'ono kwa . . . osati kutsutsa, koma kusamvetsetsana pang'ono chabe. Ndipo nthawi zambiri, ine—ine sindimakhala ndi malo akumbali a utumiki wanga, monga—monga abale ambiri ena kumunda ali nawo, monga ngati wailesi ndi televizioni, ndi magazini ndi zina zotero. Ndipo potero, bwanji, wina anganene kuti, “M'bale Branham adzakhala kuno.” Tsopano ine ndalengezedwa mmalo atatu sabata ino, lero lokha, malo atatu osiyanasiyana. Oyamba kumusi ku Kentucky, achiwiri ku California, amene ine ndikuwadziwa. Ndipo palibe chimene iwe ungachite za izo, chifukwa ndiribe malo ena ovomerezeka olengezera, chotero izo zimakhala ngati zondivuta.

⁷ Ndipo, eya, ngati pangakhale winawake wochokera uko kuzungulira Madisonville, Kentucky, kuno. Ine ndinalengezedwa kuti ndikakhala kumusi kumeneko sabata yatha, ndipo ine sindinadziwe kalikonse za izo. Ndipo ine ndinabwera kunyumba, ndipo—ndipo iwo anali atalengeza izo; ndipo m'bale amene anachita zimenezo, dzina lake Epply's. Kapena, ine ndikukhulupirira limenero linali dzina lake. Ndi chikhulupiriro chonse chabwino, iye anachita zimenezo. Iye anandiyimbira foni ndipo anandifunsa ngati tingapite kumusiko kuti—kuti tikakhale mdalitso ndi kulandira mdalitso kuchokera kwa anthu ake. Ndipo iye anayimba foni. Ine ndinamuuza iye kuti amufunse M'bale Moore. Chabwino, ndiye, ndimayenera ndizichokapo. Ndinamuuza iye kuti ndimayenera kuti ndizinyamuka tsiku lomwelo. Chabwino, M'bale Moore analephera kuti amudziwitse aliyense. Ndipo pamene, kapena kundidziwitsa ine, kapena kumudziwitsa mkazi wanga. Chotero ine ndinali uko ku Idaho, ndipo ndangobwerera kumene, ndipo msonkhano unali uli mkati.

⁸ Chotero, ndipo chotero ine ndinawona, mkati mwa izo, sangapange zokonzekera mu Louisiana pa zinthu zimene zikuchitika kuno. Chotero, ine ndinangotenga zokonzekerazo ndekha, kuti ndipange kukonzekera kwanga kwa misonkhano, mpaka misonkhano yanga yakhala. . . Ine basi ndinakhala ngati . . . Oh, sindikudziwa, ndikuganiza kuti kuvomereza ndikwabwino kwa moyo. Kodi inu simukuganiza chomwecho? Ndakhala wochedwachedwa kwambiri pa zinthu izi. Ndi kungomulolera aliyense, kulikonse, kungozisiya izo zizipita mwachisawawa. Ndipo ndinapeza kuti, izo ziribe phindu. Pakapita nthawi yaitali, inu mumaika . . . Mukuyenera kukhala ndi dongosolo lina kwa izo. Ndipo tsopano ndikuyesera kupanga zokonzekera.

⁹ Ndipo ine—ndipo ine ndikawawona Akazi a Arnold. Ine . . . Pali mwamuna muno mu Louisville amene wakhala wabwino

kwambiri, pamene ine ndinali ndi misonkhano kuno, ndipo dzina lake ndi M'bale Burgum. Ndipo iye ankafuna a—usiku umodzi kapena uwiri, msonkhanowo. Ine ndimuwona Teddy wake wamng'ono, ine ndikukhulupirira, Teddy Arnold. Kwa kanthawi sabata ino.

¹⁰ Ndiyeno Loweruka ndi Lamlungu likubwerali, ngati ine ndingathe, Ambuye akalola, ine ndikufuna ndikakhale ku Madisonville. Iwo anali ndi atumiki twente-faivi, sarte kunja kumeneko. Onse a iwo atakhala pamenepo, anabwera kuchokera... Mmodzi anali mailosi sikisi, seveni handiredi. Chabwino, panalibe aliyense kumeneko, chotero kunalibe kumeneko, ndipo silinali vuto langa, koma ine basi... koma basi kudzera mu kusamvetsetsana, kapena kunyalanyaza kumuyimbira iye. Ndipo ine ndiyesetsa kukakhala kumeneko sabata yamawa, Ambuye akalola.

¹¹ Ndiyeno, pa faivi mpaka sikisi, ine ndidzakhala ku Brooklyn, New York. Ndiyeno kuyambira pamenepo, mpaka pa fortini, fifitini, ndi sikisitini, ku Parkersburg, West Virginia. Ndinangopanga kukonzekera kuwiri kumeneko usiku watha ndi mmawa uno. Tsopano, Charlotte, South Carolina, wangokhala pa mndandanda, koma ine sindikudziwa. Kenako, maholide akubwera.

¹² Kenako ife tidzapita ku Gombe la Kumadzulo, kumene iwo akukonza a—msonkhano wamuholo yayikulu. Tsopano, iyi ndi—ndi misonkhano yaing'ono monga ku masukulu apamwamba ndi zinthu monga zimenezo. Umodzi wa uko ku Gombe la Kumadzulo, udzakhala a—mizinda iwiri, msonkhano wa mu mzinda wophatikizana, wa Oakland ndi San Francisco.

¹³ Ndipo kenako nthumwi za ku Phoenix, pokhala kuti M'bale Roberts sangakhale kumeneko chaka chino, ine ndikuyenera kukhala ngati ndatenga malo ake uko ku Phoenix, mu—mu msonkhano wonse wachigawo cha Maricopa. Ndiko kuyesetsa kwa mgwirizano.

¹⁴ Ndipo muzindipempherera ine chifukwa ine—ine ndikuwasowa iwo. Ndipo ndikuzindikira kuti nthawi iliyonse chikhulupiriro chikadziyika chokha, mdierekezi amatembenezira mfuti iliyonse mu gehena pa izo, monga choncho, inu mwaona, chotero izo zimapanga izo kukhala zovuta kwambiri.

¹⁵ Chotero, mmawa uno, kuti ndipempherere odwala. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge ena a Mawu a Mulungu Amuyaya, ndi kuyankhula mphindi pang'ono chabe kuchokera m'Malemba, ndipo kenako tidzakhala ndi pemphero la odwala. Oh, momwe ine ndimakondera kuyankhula za Iye! Sichoncho inu? Ine ndimangokonda kuyankhula za Iye.

¹⁶ Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Baibulo, Mafumu Achiwiri mutu wa 2, ndime ya 12, gawo la iyo.

Ndipo Eliya anaziwona izo, ndipo . . . anafuula, atate Anga, atate anga, magareta a Israeli, ndi apakavalo ake.

¹⁷ Ndipo tsopano mwanjira ya a—mutu, kapena phunziro, ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa: *Mwinjiro Wosiyiridwa*. Chotero Ambuye awonjezere madalitso Ake pamene ife tikuyankhula kwa inu mmawa uno. Ndipo inu mukhale mu pemphero chifukwa cha ife.

¹⁸ Pa nthawi imeneyi ya ulamuliro wa Israeli mdzikolo. Israeli linali fuko, ndipo ilo linali fuko lamphamvu, ndipo iyo inali ngati nthawi yamtendere pakati pa gawo lankhondo la ilo. Koma mu—gawo lauzimu la ilo, iyo inali ngati a—nthawi ya—za kutsanzira. Ndipo ngati tingayang’ane mmbuyo ku Chipangano Chakale, ife nthawizonse tikhoza kupeza zitsanzo za chimene chikuchitika lero. Nthawizonse, mu Baibulo, zinthu zimene ziripo tsopano, zimangokhala zoimiridwa chabe za zimene zinali pachiyambi.

¹⁹ Tsopano, Bukhu la Genesis limatulutsa chirichonse chimene chiripo mdziko lero. Palibe kalikonse mdziko koma kamene sikanayambe mu Genesis, pakuti icho ndi chiyambi. Mmenemo, munayambika lingaliro lililonse. Mu Genesis, munayambitsa chirichonse chimene chinayamba. Ndipo Mpingo wookhulupirira wabodza anayambira mu Genesis. Ndipo wokhulupirira wabodza anayambira mu Genesis. Ndipo kusayanjanitsika kunayambira mu Genesis. Genesis anali chiyambi.

²⁰ Ndipo tsopano mu ulamuliro wa Eliya, kapena ulendo wa Eliya pano pa dziko lapansi, amene anali mneneri wa Mulungu wa oralo.

²¹ Ndipo Mulungu sanadzisiye Yekha pa dziko lapansi wopanda mboni. Mulungu wakhala nthawizonse, kwinkwakwe, malo ena, amakhala ndi munthu amene Iye amatha kuyika manja Ake ndipo amatha kuyima ngati mboni. Chotero ngati Iye anachita zimenezo, kuyambira ku Genesis, pachiyambi, ndithudi, penapake, Mulungu ali naye munthu amene Iye akhoza kuyikapo dzanja Lake pa iye tsopano. Pakuti Iye—Iye ndi woposa munthu mmodzi tsopano, Iye ali ndi amuna ambiri amene Iye akhoza kuyikapo dzanja Lake, chifukwa ife tikubwera ku—ku nthawi yosonkhanitsa, nthawi yokolola.

²² Genesis inali kudzala kwa mbewu, ndipo zaka sikisi sauzande izi zakhala kukhwima kwa zokolola. Ndipo tsopano mbewuyo yasanduka mbewu iyoyokha. Iyo yabwerera ku duwa, ndipo kuchokera pa duwa kupita ku—ku chipatso. Ndipo ndi nthawi yosonkhanitsa tsopano, nthawi yokolola, zinthu zazikulu zonse zimene zinayamba. Mpingo wookhulupirira umene unayamba mu Genesis wafika ku nthawi ya chipatso, chipatso cha Mzimu. Ndipo wotsutsakhristu amene anayamba mu Genesis watsikira ku chipatso chake. Ndipo ife tiri basi mu nthawi yotsekera ya nyengo yonse ya dziko lino, a . . . ya munthu wachivundi. Ndipo ndife . . . Ndi nthawi yayikulu imene aliyense, kapena

aliyense pa usinkhu uliwonse, anayamba wakhalapo, ndi nthawi ino. Ndi nthawi yogwedeza. Ndi nthawi yovuta kwa ochimwa, koma ndi nthawi yabwino kwa Akhristu, chifukwa ife tikudziwa kuti ife—ife tikunyamula, kapena tikusonkhanitsa kuyesetsa kwakung’ono kotsiriza pamodzi, kuti tizipita Kwathu ndi kukakomana ndi Ambuye.

²³ Tsopano anthu, lero, pamene mukuyang’ana pozungulira ndi kuwona vuto lalikulu ndi kupanikizika kumene kwayang’anizana ndi fukoli, kumene...Mausiku angapo apitawo, ine ndimayankhula ndi winawake, anali mmodzi wa olondera awa amene amayang’anira, ndipo iwo anati, “M’bale Branham, ife tinangowazidwa ndi boma kuti tisamauzenso anthu kuti azigona pansu pa...kutali ndi zenera pansu, ngati bomba liphulika, kapena osapita ku chipinda chapansi, chifukwa bomba latsopano ili akhoza kuliwongolera pa walesi kuchokera ku Moscow kupita ku Fourth Street mu Louisville, ndi kukaphulitsa pa msewu, kuwombera iwo, ilo liri ndi phula...zinthu mkati mwake, mabomba, ndipo izo zimatengera ilo masauzande *ochuluka kwambiri*, masauzande *ochuluka kwambiri*, molondoleredwa ndi nyenyezi ndi zopimira, ndi kudzaligwetsera ilo ndendende pa Fourth Street mu Louisville, kuchokera ku Moscow, Russia, ndipo pamene ilo lingagunde kumeneko, samasowa kugwiritsa ntchito ndege kapena kalikonse, amangolinyamula ilo mwachangu *apa*, ndipo ilo lidzatera *kumeneko*, ndipo ilo lidzaphulitsa nthaka, ya mderalo, kuya kwa mapazi handiredi ndi sevente-faivi kwa fifitini sikweya mailosi kumene ilo likupita, fifitini sikweya mailosi.” Palibe choti nkuchita koma kukonzekera kukwera kupita mmwamba, ndi chinthu chokha choti muchite pamene nthawi zimenezo zifika.

²⁴ Tangoganizani, iwo akhoza kuwombera fifite a iwo, kapena handiredede a iwo, pa nthawi imodzi, ngati iwo atafuna kutero. Zonse zimakhala zitatha, mkati mwa danga...Ine ndikukhulupirira ndi maminiti sikisite kapena eyite, kapena chinachake, kapena masekondi—masekondi, kani, kuchokera uko kufika kuno, mpaka ku chiwonongeko chonse cha chinthu chonsecho kukhoza kuchitika. Sipangakhale chirichonse chotsalira pakati pa Louisville ndi Henryville, ndi pakati pa Louisville ndi—ndi Bardstown, kapena kumusi uko, koma dzenje limodzi mu nthaka ndi mulu wa fumbi uli mmenemo. Ndizo zonse zimene zingatsalire, pambali pa madera amene ilo lingapiteko, ndi kukawotcha kwa mailosi ndi mailosi ndi mailosi kupitirira pamenepo. Ndipo pamene lina likugwera pamenepo, lina likugwera kwinkwawake, kukakomana nalo ilo.

²⁵ Ndine wokondwa kwambiri kuti tiri ndi Pothawirapo. “Dzina la Ambuye ndi Linga lolimba, olungama amathamangira mwa Ilo ndipo amapululumuka.” Ziribe kanthu ndi mabomba angati kapena zingati china chirichonsecho...Timakhala

otetezeka Kumeneko. Chotero, dziko ndi wochimwa, posakhala ndi Pothawirapo apa, kapena Malo otetezeka awa, ndi nthawi yogwedeza. Ine ndikukhulupirira, ndikanapanda kukhala Mkristu, ine ndikanapenga, poganizira chimene chingachitike nthawi iliyonse. Ndipo ndi nyumba yodzaza ndi ana aang'ono, ndi chirichonse, ine sindikanadziwa choti ndichite. Koma ndine wokondwa kwambiri kuti ndikhoza kuyima mnyumba mwanga ndi kuwadziwitsa iwo Pothawirapo pamene palibe bomba limene lingakhudzepo, kapena china chirichonse, pansa pa Mapiko oteteza a Ambuye Yesu. “Osati ndi mphamvu, osati ndi nyonga, koma mwa Mzimu Wanga,” atero Yehova. Mukuona? Ndicho chitetezero chathu.

²⁶ Ndipo ndi nthawi yayikulu bwanji, yaulemelero imene iyo ili, kudziwa kuti tchimo lonse ndi zovutika ndi mayesero a moyo posachedwapa zidzatha. Izo zonse zidzatha limodzi la masiku awa, ndipo ife tidzapita Kwathu kukakhala ndi Ambuye. Tsopano, chimene chatsalira ndi nthawi yolalikira Uthenga ndi kubweretsa mu Nsanja yayikulu iyi ochuluka, ochuluka monga momwe tingathere.

²⁷ Ndiyeno, pamene tikuwona kachitidwe ka phunziro lathu lero, la Eliya, mu ulamuliro wake, iye...kapena, ulendo wake pa dziko lapansi, bwanji, iye anali mwamuna wamkulu, wamphamvu. Mulungu ankamugwiritsa iye ntchito mwa njira zamphamvu, ndi mphamvu zazikulu. Ndipo ife tikupeza kuti mu nthawi iyi, panali gulu la otsanzira amene ankayesera kumutsanzira Eliya, amene ankayesetsa kuchita zinthu zomwezo zimene Eliya ankachita.

²⁸ Ndipo chotero ife tikupeza chinthu chomwecho lero; kutsanzira kwa Chikristu, anthu amene amayesetsa kumachita ngati Akristu, amene amayesetsa kudzipanga okha Akristu. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Mulungu ayenera kuchita zimenezo. Iye ndi Mmodzi yekhayo Amene angathe kuchita zimenezo.

²⁹ Chotero iwo anapanga sukulu, ndipo anaitcha iyo, “sukulu ya aneneri.” Ndipo iwo onse anapita ku sukulu ya aneneri, ndipo iwo anakawaphunzitsako iwo. Ndipo ine ndikhoza kulingalira alaliki onsewo kumtunda uko, atavala mtundu womwewo wa chikhotho chimene Eliya ankavala. Ine ndikukhoza kulingalira akuyesetsa kuti amutsanzire iye pa liwu lake, momwe iye ankayankhulira. Ndi—ndi momwe iye ankadziwonetsera yekha, aliyense kumayesetsa kuchita chinthu chomwecho, chifukwa Eliya anali munthu wamkulu wogwiritsidwa ntchito ndi Mulungu.

³⁰ Ndipo ife tikupeza chinthu chomwecho lero. Ine ndimamvetsera kuwulutsa kwa pa walesi, osati kale kwambiri. Iwo ali ndi a Billy Graham konsekonse mdziko muno, kuyambira pamene Billy anali mu Louisville. Aliyense kumayesetsa

kutsanzira chinthu chomwecho, pafupifupi kupesa tsitsi lawo mofanana, ndi—ndi kuvala chinthu chomwecho, ndi liwu la mtundu womwewo, ndi zina zotero. Koma inu simungakhoze kuchita zimenezo. Inu mukuyenera kukhala chimene inu muli ndi chimene Mulungu anakupangani inu kuti mukhale. Uko nkulondola. Ndipo chotero ife tikupeza momwe izo, mwinamwake, mmasiku amenewo chinthu chomwecho chinachitika.

³¹ Tsopano, Mulungu, powona, powoneratu kuti masiku a Eliya anali owerengeka, kuti anali ndi nthawi yaitali kuti akhale padziko lapansi, monga momwe aliyense wakhalira. Chotero, Iye anali wakuti akhale ndi wolowa mmalo mwa Eliya. Ndipo pamene Iye anatero, Mulungu anamuyitana munthu uyu. Iye sanali mu seminare pamene Iye ankamuyitana iye. Iye anali akulima mmunda, ndi goli la ng'ombe, akuchita utumiki, kapena kusamalira amayi ndi abambo ake. Ndipo Mulungu anamuyitana iye kuti adzakhale wolowa mmalo mwa Elisha, kapena Eliya.

³² Mwinamwake ambiri pa sukulupo ankaganiza ndithudi kuti adzakhala wolowa mmalo mwake, iwo akanadzavala mwinjiro wake iye akadzangothana nawo iwo.

³³ Koma, Mulungu amachita kuyitanako. Mulungu amachita kusankhako. Mulungu amachita kusankha. Mulungu amachita kuyika mu dongosoloko. “Mulungu anayika mu Mpingo: ena, atunwi; ena, aneneri; ena, aphunzitsi; ena, avangeri; ndi azibusa.” Mulungu amachita zimenezo, Iyemwini. Sitingathe kupangitsa tsitsi limodzi kukhala lakuda kapena loyera, ndiponso ife sitingathe kuwonjezera kanthu kamodzi pa thunthu lathu potenga lingaliro. Mulungu, mu chisomo Chake chopanda malire, ndi mwa kusankha Kwake ndi kudziwiratu Kwake, anaziyika zinthu izi mu dongosolo, ndipo gudumu lililonse limagwira ntchito bwino basi. Ine ndikuzikonda zimenezo.

³⁴ Ine ndingakhale munthu wokhumudwitsidwa, mmawa uno, ngati ine ndikanati ndisamakhulupirire mu kusankha ndi kuyitana kwa Mulungu. Ngati nditamaganiza kuti dziko lino linasiyidwira ku mathero ake, ndi mphamvu za munthu, ndi nzeru za munthu, ndi pa “zazikulu zinayi,” ndi a U.N., ndipo amene samatchula nkomwe Dzina la Mulungu, ine ndingakhale munthu wokhumudwitsidwa. Koma sindikuyang'ana izo ngati zotsatira zake.

³⁵ Ine ndimayang'ana pansu mmasamba a Bukhu lakale ili *apa*, mmene Mulungu anazilemba Izo, ndipo chirichonse chidzabwera ndendende basi momwe Iye ananenera izo, ndipo ndizo zonse. Chotero, chinthu chokha choti ine ndizichita si kugwirizana ndi iwo, koma kugwirizana ndi Kalvare. Kugwirizana ndi Mulungu, kugwirizana ndi Mawu Ake, kumakhala mu Mawu Ake. Ziribe kanthu momwe izo zikuwonekera ngati izo zikhala *choncho*; izo zikhala momwe

Mulungu akufunira kuti izo zikhalire. Izo sizingakhale china chirichonsecho. Pakuti, Iye pokhala wopandamalire, ankadziwa mathero kuchokera ku chiyambi, ndipo Iye amapangitsa chirichonse kubwera ku matamando Ake. Uko nkulondola.

³⁶ “Zinthu zonse zikuyenera kugwirira ntchito limodzi.” Chirichonse chikuyenera kuwumbika mpaka kukafika pamalo ake. Mai! Ngati izo sizingapange kulimba mtima mwa Mkhristu! Palibe chimene chingasokonezeke. Pambuyo pake, si nkondo yathu; ndi Yake. Si nzeru zathu; ndi Zake. Chinthu chimodzi chokhacho chimene ife tinkayenera kuchita ndi kuyika chikhulupiro chathu ndi chidaliro pamenepo, ndi kukhala chete ndi kumawona ulemelero wa Mulungu, mwaona momwe Iwo amasunthira mozungulira kupita ku malo Ake, ndipo gudumu lililonse kumayenda. Iwo akhoza kumwazikana mbali ndi mbali, koma Iwo adzasunthira kumene mpaka kumalo Ake oyenera pamene Mulungu ayankhula Mawu.

³⁷ Iye anadziwa mapeto kuchokera kuchiyambi. Iye ankadziwa kuti adzasankha. Iye ankadziwa kuti Elisha akanadzatenga malo a Eliya, dziko lisanawumbidwe nkomwe. Chirichonse chikuyenera kugwira ntchito ndendende molondola.

³⁸ Ndipo ife timakhala ndi nkhwana ndi okonedwa athu, ndi zina zotero, “Kodi iwo adzalowa?” Maina awo, ngati iwo analembedwa mu Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, iwo adzagwira ntchito yobwera pamenepo. Ndicho chinthu chokhacho chimene iye angachite. Ife timachitira umboni ndi kuwalitsa Kuwala. Mulungu amachita, ndi Mmodzi amene amakubweretsa Iko kwa iwo.

³⁹ Tsopano zindikirani, mwa Eliya, ndiye, iye ataponyera mwinjiro wake pa iye, ndipo anawuyesa iwo pa iye. Mwa kuyankhula kwina, Eliya mneneri, amene anali ndi chovala cha Mulungu pa mapewa ake, iye anatsika ndipo anadzachiika icho pa Elisha, mlimiyo, kuti awone ngati icho chingamukwane iye. Ndipo zinatengera pafupifupi zaka teni kuti asinthidwe, kuti akwanire mu chovala chimenecho.

⁴⁰ Inu mukudziwa, Mulungu nthawi zambiri amatiyika mu sitolo ndi kumatikonza ife. Tsopano, Iye sanasinthe mwinjiro wake kuti umukwane Elisha; Iye anamulamulira Elisha kuti akwane mu mwinjirowo. Ndipo ndicho chimene Iye akuchita lero. Iye amatisintha ife kuti tikwaniremo mu mwinjirowo, osati mwinjiroyo itikwane ife. Nthawizina timafuna kuti mwinjirowo utikwane, koma sitingathe kuchita zimenezo. Inu mukuyenera (kulola) kusinthidwa, inueni, ku mwinjirowo. Ndi mwinjiro wa Mulungu, ndipo Iye anawupanga iwo wangwiro. Ndipo ife tiri. . . Iye akuyenera kutibweretsa ife mu gawo limenero, kuti awupange mwinjirowo utikwane ife.

41 Chotero, ife sitingakhale angwiwo, tokha. Ife tikudziwa kuti sitingathe. Palibe njira yoti ife tingakhale, ndipo, komabe, Iye ananena kuti ife tikhale. Chotero, koma, chimene Iye anachita, Iye anapanga chitetezero kwa ife; Ambuye Yesu Khristu ndi chirungamo Chake. Ndiko kumene ungwiwo umachokerako; za kusalabadira chiyero chatu chomwe, chimene ife tiribe nkomwe; ndi malingaliro athu omwe, amene sakuyenera kukhalapo. Koma ife timapumula mwaulemu pa ntchito yomalizidwa ya Ambuye Yesu. Mulungu anamutumiza Iye pa dziko lapansi, ndipo munali mwa Iye mmene ife timapumulamo.

42 Zindikirani, zaka zonsezi, monga momwe ife tikudziwira, iye anangokhala ndi ubatizo umodzi uwo wa mwinjiro ukupita pa iye. Koma kudutsa mzakazi, Mulungu anali atawumba khalidwe la munthuyo kufika pamalo akuti, atatha kuyitanidwa, kuti akanadzakwanira mu mwinjiro ndi kudzakhala mtumiki wa Ambuye.

43 Ndiyeno pamene Eliya anadutsa ndi kudzaponyera icho pa iye, ndipo iwo ananyamuka kumapita ku Giligala ndi malo ena ambiri amene iwo anapitako, mpaka ku sukulu ya aneneri, pa ulendo wawo, akuyenda mopitirira. Ndipo, potsiriza, Eliya ankayesetsa kuti amupangitse Elisha kuti abwerere mmbuyo. Kodi inu munazindikira zimenezo? Kuyesetsa kuti amupangitse iye kuti abwerere mmbuyo. Anati, “Ine . . .” Apo ayi, “Mwinamwake msewu ndi wotsetsereka pang’ono kwa iwe, mwana. Mwinamwake ndi wopapatiza pang’ono kuti iwe uyendemo.”

44 Inu mukudziwa, kumene kunali Eliya, kunali kuwongoka. Ndipo kulikonse kumene wantchito woona wa Mulungu amalalikirako Uthenga, umakhala Uthenga woongoka, wosaipitsidwa kumene Iwo ukulalikidwako.

45 Bwanji, tsiku lina, iye anapita uko ku sukulu ya aneneri, kuti akawachezere iwo, ndipo iwo anamupempha iye kuti azipita. Iwo anati, “Ndi zolunjika kwambiri pano, kwa ife.”

46 Chimene ife tikusowa lero ndi kulalikira kwina kolunjika, kulalikira kwa Uthenga kumene kudzalekanitse tirigu kwa mankhusu, kapena chabwino kwa choyipa. Kupangitsa chimene chiri choona “choona,” ndipo chimene chiri cholakwika ndi “cholakwika.”

47 Anthu onsewa ndi zowachitikira zawo, ndi zonse zimene iwo anali! Iwo anapita kuti akapeze chinachake choti adye, ndipo mmodzi wa iwo anapeza mphesa zakuthengo, ndipo anatolera zipuzi zina zakuthengo, ndipo anaphika imfa ina mumphika wawo wachipembedzo. Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anafuula, “Muli imfa mu mphikamu!”

48 Koma Eliya, ndi magawo awiri, ankadziwa choti achite, chotero iye anayika ufa wodzaza dzanja mu mphikamo. Anati, “Tsopano tiyeni mukadye izo.” Mwa kuyankhula kwina, iwo . . .

⁴⁹ Lero, choyimira, ine ndikhoza kuganiza, kuti ife tiri ndi Amethodisti ambiri, Abaptisti, Apresbateria, Achilutera, Achipentekoste, ndi china chirichonse, zonse zitasakanizidwa pamodzi, ndipo wina kumamenyana ndi mzake. Ndipo ife sitikusowa kuti tichichotse chinthu chonsecho ndi kuthana nacho icho. Ife tikusowa Ufa wina wodzaza mdzanja. Kusunga mpingo womwewo.

⁵⁰ Ufawo unali wochokera m'nyumba ya sukulu kumeneko, imene inali nsembe ya ufa imene anthu ankabweretsa, ndi zipatso zoyambirira za zokolola zimene zinaperedwa ndi mano ena ake amene anapangitsa njere iliyonse ya ufa kukhala yofanana. Ndipo kenako pamene. . .

⁵¹ Ufa uwu, pokhala wofanana, unali choyimira cha Khristu. Ufa ndi moyo. Ndipo pamene choyimira cha Khristu, ufawo, pokhala woperedwa mofanana; kutanthauza, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ndipo ufa mu nsembe ya ufa, ndipo pamene iwo anayika ufa uwu mmenemo, kumuyika Khristu mu imfa zinabweretsa Moyo. Ndicho chimene chimapangitsa kusemphana mmawonekedwe athu akufa, mu kutsemphana kwathu, mmikangano yathu yachipembedzo ndi chirichonse. Ngati titangomubweretsa Khristu mu zimenezo, izo zingasinthe imfa, ndipo nkutilekanitsa, kukalowa mu Moyo, ngati titangochita zimenezo.

⁵² Alipo Abaptisti naintini milioni mu Amerika. Alipo Amethodisti sartini milioni mu Amerika. Alipo Achilutera leveni milioni mu Amerika. Ndiponso Achipresbateria teni milioni mu Amerika. Ndipo Mulungu amangodziwa ndi Akatolika angati, amene amaposa chipembedzo chirichonse. Koma, mu zonsezo, kodi ife tikusowa chiyani? Ufa wodzaza mdzanja. Ife tikuyenera kubweretsa Moyo ku mpingo. Ndipo Khristu ndi Moyo. Iye anabwera kuti adzatibweretsere ife Moyo.

⁵³ Chotero, iwo anali ndi mikangano yawo, ndi masukulu awo, ndi zawo zafio-. . .zafioleje, ndi zina zotero.

⁵⁴ Ndipo kenako Eliya anamuza Elisha, “Kulibwino ubwerere mmbuyo, chifukwa njirayi ikhoza kukhala yovutirapo pang’ono.” Koma munthu wa Mulungu amene anakomano nazo izo, kapena anaponyedwera paphewa pake mwinjiro wa chirungamo cha Mulungu ndi mphamvu, sizophweka kwambiri kumubwenza mmbuyo.

⁵⁵ Pamene ine ndinawamva abusa akunena, mmawa uno, kuti athu. . .“Ambiri akukhumudwitsidwa.” Chimene ife tikusowa, m’bale, ndi kulimba mtima! Chimene ife tifusowa ndi kulimbikitsidwa, zoonza zimenezo. Mayesero akhoza kubwera. Sitalonjezedwe kuti tidzatetezedwa kwa iwo, koma Iye adzapereka chisomo kuti tidzadutse mwa iwo. Ngati phirilo lili lalitali kwambiri kuti tilidumphe, lakuya kwambiri kuti tipite pansu pake, lotambalala kwambiri kuti tipite molizungulira

ilo, Iye adzapereka chisomo kuti mudutsemo. Zoona zimenezo. Musadandaule basi, koma muyike maso anu pa Khristu, pakuti Iye ndi Mmodzi yekhayo amene angathe kutidutsitsa ife.

⁵⁶ Tsopano, ife tikuwaona iwo pamene iwo akuyenda, akubwera ku sukulu. Ndipo iye anati, “Iwe khala pano tsopano. Ukhale pano, ndipo ukhale pansu ndi kukhala mphunzitsi wabwino wa fioloje, ndi zina zotero. Ndipo mwinamwake, tsiku lina, udzakhoza kukhala woyang’anira koleji kuno. Koma ine ndikuyenera kuti ndipite kumusi patsogolo pang’ono.”

⁵⁷ Kodi inu mungalingalire munthu wa Mulungu kumakhutitsidwa kuti akhale woyang’anira koleji, pamene Mphamvu ya Mulungu inali pafupi ndi pamene iye anali atayima? Ayi, bwana. Iye anati, “Pali Ambuye ndipo pali moyo wako, ine sindikusiya iwe.” Ine ndikuzikonda zimenezo.

⁵⁸ Kukhala ndi chimenecho, ziribe kanthu ngakhale wokhumudwa bwanji, ngakhale zitakhala kuti zikuchokera kwa amayi anu, abambo anu, kapena kwa abusa anu. Mukhale ndi Iye.

⁵⁹ Iwo anapita mpaka ku Yordani. Iwo anakawoloka. Ndipo Eliya anati, “Tsopano, kodi iwe ukufuna kuti ndikuchitire chiyani?”

⁶⁰ Iye anati, “Magawo awiri a mzimu wanu abwere pa ine.” Iye ankadziwa kuti iye anali ndi ntchito yoti achite. Iye anati, “Magawo awiri.” Osati chongondichitikira chabwino chofunda, osati kugwirana chanza kwabwino kokha, kapena chiyanjano chabwino ndi mpingo wonse. Koma, “Chimene ndikufuna ndi magawo awiri a chimene chiri chabwino kwambiri tsopano.”

⁶¹ Ine ndikukuuzani inu, pamene Mulungu amuyika munthu ku ntchito ya mdziko, iye akuyenera kukhala ndi chinachake chabwinoko kuposa chimene dziko liri nacho. Iye akuyenera kukhala ndi chinachake chabwinoko kuposa chimene mpingo uli nacho. Iye akuyenera kutsatira magawo awiri.

⁶² Ndipo ngati inayamba yakhalapo nthawi imene magawo awiri akufunika, ndi lero, mu madera a anthu; chinachake chabwinoko, chinachake chapamwamba. Ine sindingathe... Ndikuganiza kuti nyemba ndi nsima ndi zabwino kwambiri, koma nthawizina ndimayenera kufikira pamwamba pang’ono. Ndipo ife timachita zimenezo; tikuyenera kutero. Tikuyenera kuti tizipitirira kumakwera. Israeli anali kuti akubwerera mmbuyo ngati iye akanamapitiriza kukhala pa nthaka yomweyo. Iye akuyenera kumasunthabe kapena kubwerera mmbuyo. Ndipo umo ndi momwe mpingo uliri.

⁶³ Chotero, pamene iwo ankapita, sizinali koma maminiti pang’ono mpaka iye anati, “Iwe wapempha chinthu chachikulu, koma, komabe, ngati iwe udzandiwona ine pamene ndizidzapita, udzakhoza kulandira chimene wapemphacho.”

⁶⁴ Tsopano, icho chikuyenera kukhala umodzi wa cholinga, mwa mtima umodzi, umodzi wa diso, kusunga diso lako pa lonjezo. Hum! Ngati inu mukudwala mmawa uno, ngati inu mukusautsika, pali lonjezo limodzi lalikulu; osati mwa Eliya, koma mwa Mulungu Iyemwini. “Ngati inu mungakhulupirire, pamene inu mupemphera, mukhulupirire kuti inu mulandira chimene inu mwapempha, ndipo inu mulandira icho.” Ziribe kanthu chimene dokotala akunena, mochuluka momwe *ichi* chikupitira kapena *icho* chikupitira; mukhale mmodzi pa lonjezo.

⁶⁵ Eliya anamupatsa iye ntchito, “Ngati iwe udzandiwona ine pamene ndizidzapita, izo zidzabwera pa iwe.”

⁶⁶ Ndi limenelo lonjezo, “Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira.”

⁶⁷ Nthawizina ndimadziyang’ana ndekha, ndipo ndimaganiza, “Ndakhala nsomba yopanda minga mmoyo wanga. Ine ndadikirira, ndipo ndaphonya masauzande a miyoyo yambiri, kulowa mu Ufumu, chifukwa ndimadikirira ndikuti, ‘Mulungu...’ Ndinkadalira kwambiri pa mphatso yauzimu. Ndikumati, ‘Ambuye, ngati Inu mungandiwonetse ine, ngati Inu mungandipatse ine masomphenya a choti ndichite.’” Ndipo Mulungu nkupereka masomphenyawo, ndiye ine nkutembenuka ndi kumulola winawake kuti andiyankhule ine kulowa mu chinachakenso.

⁶⁸ Ndipo, oh, ine sindinafike pamalowo, panobe, mpaka ine . . . monga ine ndachitira pa nthawi ino, kuti ine ndikumverera kuti ndi chikhulupiriro, kuti ife tikuyenera kutulukira kunja uko, chifukwa ndi lonjezo. Ndi zinthu zimene Iye wazichita, ndi machiritso amene Iye wachita, ndi zozizwitsa; mochuluka, wabwera pansu ndipo anajambulidwa chithunzi Chake pambali pa ife, ndi zina zotero, zimene sizinadziwikepo chiyambire dziko lapansi. Ndiyeno nkuimirira pamenepo ngati nsomba? Mpaka zimandipangitsa ine kukhumudwa ndi inemwini. Ndi nthawi yoti muyang’ane pa lonjezo.

⁶⁹ Ndipo ndicho chimene, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndikulinga kuti ndichite. Ndipo ine ndikuzindikira kuti mdierekezi aliyense wa ku gehena awombera icho. Koma, mwa chisomo cha Mulungu, ndikulinga kuyika diso langa pa lonjezolo.

⁷⁰ Elisha anati, “Ngati iwe,” kapena, Eliya anati, “Ngati iwe udzandiwona pamene ndizidzapita, iwe udzapeza chimene wachipempha.” Uko nkulondola. Inu mukuyenera kuyika diso lanu pa zimenezo; kuyang’ana lonjezolo. Monga, bwanji ngati ena a sukulu, ngati atabwerera, ndi kuti, “Heyi, anyamata, ndikuchita bwanji tsopano, ndikutsatira kumbuyo komwe kwa mneneri?” Iye akanalephera, mwinamwake. Koma iye sanasamale chimene sukuluyo inkaganiza, kapena chimene

aziphunzitsi onse ankaganiza. Iye sanasamale chimene oyandikana nawo ankaganiza, kapena nyumba, kapena amene ankamuyang'ana iye. Iye anayikabe chikhulupiriro chake mu lonjezolo.

⁷¹ Chimene ife tikusowa lero ndi chikhulupiriro mu lonjezo la Mulungu, ndipo osakhala ndi chidwi ku chimene *uyu* akunena kapena *uyu* akunena.

⁷² Monga m'bale ananena, mtumiki anali ndi atsikana awiri amene anali osayankhula, ndipo kutsutsa pa machiritso Auzimu, kumati, "Anawo sangathe kuchiritsidwa."

⁷³ Musapereke chidwi kwa otsutsa. Muyike chikhulupiriro chanu pa lonjezo. Mulungu ananena choncho! "Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala, ndipo Mulungu adzawaukitsa iwo." Ngati Iye angathe kumupangitsa mmodzi wogontha kuti adzimva, Iye akhoza kumupangitsa wina wogontha kuti adzimva. Ife tikudziwa, mwa zitsimikizo zosalephera, kuti Iye amachita zimenezo. Tikhazikitse chikhulupiriro chathu pa lonjezolo. Maso athu amodzi; makutu athu amodzi; mitima yathu imodzi; ndipo, chinthu chimodzi, pa Yesu Khristu, ndipo Iye ndi wokhoza kuchita chimene Iye walonjeza. Oh, pamene ife tiganiza za zimenezo, izo zimasintha chochitika chonse pamene ife tipeza izo. Mulungu anapanga lonjezo. Mulungu anali Mmodzi amene ananena izo.

⁷⁴ Tsopano, *apa* panali woyimira Mulungu ananena izo, ndipo tsopano Mulungu Mwiniwake wanena izo. Ndiye ife tingachite chiyani? Palibe koma kuyika malingaliro athu pa izo. Anati, "Ngati iwe udzandiwona ine ndikupita, iwe ukhoza kudzakhala nalo lonjezolo." Elisha anayika maso ake pa Eliya. Zinalibe kanthu zimene zimafuula kuchokera mbali zonse, zimene zimachitika mbali zonse, zimene zinkachitika izo zisanachitike, iye samayang'ana nkomwe pa zimenezo. Iye anayika maso ake pa lonjezolo. Ndi zimenezotu, maso anu pa lonjezo.

⁷⁵ Ine ndikuganiza za dona yemwe tinamuchezera usiku wina, Mlongo Sauer. Ndipo dokotala akumuuzza iye momwe iye anali atayipira. Ndipo ine sindinamuwuze konse iye; ndinamuuzza wokonedwa wake. Ndi momwe zinaliri zosatheka kuti iye achire konse. Tsopano, m'bale, mpongozi wake anandifunsa ine za izo. Ine ndinati, "Ngati iye angayike maso ake pa lonjezolo." Ziribe kanthu chimene chingachitike, muike maso anu pa lonjezo.

⁷⁶ Masabata pang'ono apitawo, Mlongo Wood kuno, ndi M'bale Wood, amzanga awiri apamtima athu kuno ku tchalitchi. Ine ndinali ku Michigan ndi azimzanga, Leo ndi Gene. Ife tinali titachoka ku msonkhano waku Chicago ndipo tinapita ndi ena a anthu awo, ku...kwa masiku awiri, kupita kukasaka mphalapala ndi mauta ndi mivi. Ndipo ndiri panjira ndikubwerera, mkazi wanga anali atandipeza

ine, ndipo iye anati, “Muwapempherere amayi awo a Akazi a Wood. Khansa yadya nkhope yawo.” Ndipo anati, “Ine sindinamuwonapo Mlongo Wood atadzidzimuka chotero. Iye akulira.” Mlongo Wood nthawizonse wakhala ngwazi ya chikhulupiriro, kuyambira pamene Mulungu anamuchiritsa mnyamata wake mwendo wolumala, ndi kumuchiritsa iye TB, ndi zina zotero. Koma iye anali atasiya.

⁷⁷ Kumeneko kuchipinda, usiku umenewo, ife tinapemphera. Akubwera, Akazi a Wood anati, “M’bale Branham, ife tipitako.” Ndipo ife tinapita kwa amayi ake, amene anali mu Louisville. Ndipo iye anali ndi khansa pa mbali ya mphuno yake, ndipo adokotala anali ataigwiragwira iyo, anaimwaza iyo; mpaka panangokhala kuzungulira mmbali mwa mphuno yake, ndipo mmwamba basi pafupifupi eyiti ya inchi kuchokera pa diso lake, basi fupa la pamenepo. Inadya iyo mwamsanga momwe iyo ikanatha kudyera.

⁷⁸ Tinalowa mchipindamo, ndipo ine ndinagwada pansi. Ine ndinati, “Ndikufuna kuyankhulana naye yekha.” Ndipo ine ndinalowa mchipindamo kukapemphera ndi mkaziyo. Ndipo ndiri mchipindamo, ndinaganiza, “O Mulungu, ngati Inu mutangondiwonetsa ine masomphenya a chimene chiti chichitike kwa mkaziyu.” Bambo ndi Mayi Wood atakhala panja, akuyembekezera kuti awone chimene masomphenyawo akanati anene.

⁷⁹ Koma pamene ine ndinali pamenepo, ine ndinatsutsidwa. Ndinatsutsidwa podikira masomphenya. Zinkawoneka ngati Chinachake chinalozera mmbuyo, “Sikunali kuyitana. Kodi iwe ukufuna masomphenya, pamene lonjezo lanenedwa kale?” Chotero ndinagwada pansi ndipo ndinapemphera. Ndipo pamene ndinapemphera, chinachake chinangozikika mkati, chikhulupiriro cha lonjezo.

⁸⁰ Ndinabwerera panja. Ndipo Akazi a Wood, pamene ine ndinawauza iwo za izo, iwo anati, “Kodi inu munawona chirichonse, M’bale Branham?”

⁸¹ Ine ndinati, “Ine sindinawone kwenikweni chirichonse, koma ine ndinamverera Chinachake chimene chinandiuza ine kuti lonjezo Lake linali loona ndipo Iye achita izo. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Iye achita izo.”

⁸² Ndipo mu maora osachepera twente-foro, mapeto a khansa imeneyo anayamba kusweka ndipo khungu linabwera pa iyo. Khansa siikhala ndi chikhadabo, monga inu mukudziwira, pokhapokha ngati iyo yafa. Chotero apo icho chinali tsopano. Ndipo mkaziyo wachiritsidwa, ndipo ali kwawo. Ndi Khristu wodabwitsa bwanji! Poyika maso athu pa lonjezo! Mulungu ananena chomwecho!

⁸³ Koma pamene ife tipemphereredwa, nthawizina, timanyamuka ndi kukati, “Chabwino, izo sizinachitike nthawi

yomweyo, chotero mwinamwake kulibwino ife tibwerere kachiwiri.” Oh, ayi.

⁸⁴ Muyike diso lanu pa lonjezo. Mulungu wanena chomwecho, izo zikukhazikitsa izo. Ndizo zonse. Ngati Mulungu wanena chomwecho, Mulungu ndi wokhoza kusunga lonjezo Lake, kapena Iye sakanati achite zimenezo.

⁸⁵ Abrahamu anadzitcha zinthu zimenezo, zimene kunalibeko, ngati kuti zinalipo. Ndipo, kwa zaka twente-faivi, anayima pa zosathekazo, chifukwa iye ankawerengera kuti Mulungu anali wokhoza kuchita chimene Iye analonjeza. Amen. Ndipo ife ndi ana a Abrahamu, mwa chikhulupiro.

⁸⁶ Ndithudi, Eliya anayika maso ake pa . . . kapena Elisha pa Eliya, ndipo pamene iwo ankapita. Ndipo patapita kanthawi, galeta linabwera ndipo linawalekanitsa iwo, mmodzi ku mbali ina ndi wina, ndipo kenako ilo linamunyamula Eliya. Pa . . . Iye anakwera pagaleta ndipo anapita mmwamba, ndipo anachotsa mwinjiro wake paphewa lake ndipo anawuponya kwa Elisha. Chifukwa, Elisha anali atakulira mmenemo, inu mukudziwa, chotero iwo unamukwana iye moyenera. Ndipo inu mukhoza kulingalira . . .

⁸⁷ Oh, ine ndikufuna inu mundipatse ine tcheru chanu chosagawanika, pamene ine ndikumverera kukhosi kwanga kukuyabwa. Ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu chinachake.

⁸⁸ Kodi mungalingalire mmene Elisha anamverera pamene ananyamula mwinjiro uwu, nkudzawuyika iwo pa phewa pake? Oh, ndikumverera kotani!

⁸⁹ Ine sindikutanthauza izi kuti zikhale za ineyo, koma pafupifupi zaka teni zapitazo, kuchokera pa guwa pano, ine ndinalalikira pa ulaliki; Davide, wankhondo ali ndi legeni mdzanja lake, ndipo Goliati ali patsogolo pake. Mmasiku amenewo kunalibe misonkhano yamachiritso kuminda, kulikonseko, monga ife timadziwira. Ndipo, oh, momwe anthu analiri otsutsa pa machiritso Auzimu! Koma pamakhala chinachake, atha kukumana ndi Chinthucho. Ndipo azibusa anandiiza ine kuti ndimasokonezeka ubongo wanga, kuti sizimayenera kukhala chomwecho. Koma, kuchokera pa bokosi lomweli apa, ine ndinayankhula za Davide. Anati, “Kodi mukutanthauza kundiuza kuti awa, magulu a nkondo a Mulungu wamoyo, alola Mfilisiti wosadulidwa ameneyo kunyoza gulu lankhondo ili?”

⁹⁰ Mnyamata wamng’ono wamapewa akugwa, watsitsi lopiringizika atavala malaya a chikopa cha nkhosa, ndi legeni m’dzanja lake; ndi gulu lankhondo lonse la Israeli litayima, atatchingira. Ndipo iye, yekha, anatulukira. Ndi mwamuna, ndi—ndi nkondo wotalika mapazi naintini, ndipo chinthucho kumapeto kwake chinkalemera masekeli angapo, mwinamwake

ndi mapaundi twente a chitsulo, chakuthwa, nkondo wa mapazi naintini, ndi zala zotalika mainchesi fortini.

Ndipo Davide mwinamwake ankalemera mapaundi nainte, ndipo anayima, akudumphadumphapha chokwera ndi chotsika, ngati tambala wamng'ono, ndipo akuti, "Mukutanthauza kundiuza ine," oh, mai, "kuti inu mumulola Mfilisiti wosadulidwa uyo! Ngati iye wakhala pamalo ake, msiyeni iye akhale, koma iye akunyoza magulu ankhondo a Mulungu wamoyo." Oh, mai, ndi ngwazi bwanji! "Ndipo nonsenu mukuwopa kupita kukamenyana naye?" Anati, "Ndiloleni ine ndikumanizane naye iye." Oh, mai! Iye anati, "Mulungu wa Kumwamba anandilola ine kuti ndiphe mkango ndi legeni, Iye anandilola ine kuti ndiphe chimbalangondo ndi legeni, ndipo ndi mochuluka bwanji momwe adzamuperekere mfilisiti wosadulidwa ameneyo mu dzanja langa!" Ndithudi.

⁹¹ Ndipo pamene chigonjetso choyamba chinagonjetsedwa, ndipo Goliati anagwetsedwa, ankhondo onse a Israeli anamutsatira Davide. Ndipo iwo anakadula mitu ndi kukammenya, Israeli... kapena kukawamenya Afilisiti mpaka kukawafikitsa ku dziko lawo. Iwo anawapanikizira iwo mu ngodya, ndipo anawapha iwo, ndipo anatenga mizinda yawo, ndi chirichonse, ndipo anali ndi chigonjetso.

⁹² M'bale ndi mlongo, chinthu chomwecho chachitidwa mu madera auzimu, pamene iwo anati, "Machiritso auzimu sangagwire ntchito. Masiku a zozizwitsa anapita." Ngati masiku a zozizwitsa anapita, masiku a Mulungu anapita. Mpingo umene sumakhulupirira zauzimu potsiriza udzafa, ndipo Mulungu adzawusiya mpingowo. Akuyenera kutero! Ndipo Mulungu anapereka lonjezo, ndipo malonjezo a Mulungu ndi Amuyaya.

⁹³ Kuno nthawi ina mmbuyomu pamene atsikana ena ankasewera ndi rediamu, ndipo ankaviika mmenemo, ndi kumapenta mivi ya rediamu pa mawotchi. Ndiri nazo zina pa izi. Ndipo mtsikana wina analakwitsa ndipo anatenga burashi ndipo anadzaiyika iyo mkamwa mwake. Iye anamupha iye. Ndipo zaka ndi zaka mtsogolo, iwo anatenga maikrosikopu ndipo anadzawayika iwo pa chigaza cha mtsikanayo, ndipo amamumvabe rediamu ameneyo akupitirira, "Burru-burru-burru." Iye samakhala ndi mathero. Amapitirirabe kumagwira ntchito, kumapitirira ndi kupitirira. Sipamakhala poimira kwa iye.

⁹⁴ Ndipo, oh, m'bale, ngati rediamu amakhala ndi mphamvu za mtundu umenewo mwa ife, kuli bwanji Mulungu wopanda mapeto, Wamuyaya, wauzimu, wamphamvuzonse, wopandamalire, Mulungu Wamphamvuzonse! Iye akuyenera kukhala ndi mphamvu yomweyo monga Iye anayambira. Iye akuyenera kukhala ndi zonsezo, kapena Iye si Wamphamvuyonse, Mulungu Wamphamvuzonse. Iye

akuyembekezerabe munthu wa chikhulupiro cholimba, amene angatulukire ndi kumutsutsa mdani pa maziko a Mawu Ake ndi kunena kuti Izo ziri chomwecho.

⁹⁵ Ndipo tsopano chinachitika ndi chiyani, mwamsanga pamene msonkhano waukulu wa machiritso unayambika? Ndiye zikwi za asilikari, a amuna a Mulungu, amene ankakhala mmbuyo mmipingo yaying'ono, monga Oral Roberts, Tommy Hicks, ndi ambiri a amuna odziwika aku minda, anasolola Lupanga lawo ndipo anapita. Lupanga *ili* limene limadula zonse zobwera ndi zopita, mmwamba ndi pansi, ndiponso zolowa ndi zotuluka, “Wozindikira za maganizo, ngakhale mmafuta a mmafupa.” Iwo anasolola Mabaibulo awo, Lupanga lawo, ndipo anachokapo, pamene iwo anawona kuti izo zikanatha kuchitika. Ndipo ife tamumenya mdani, mwa chisomo cha Mulungu, mpaka dziko lonse lakhala ndi chitsitsimutso cha machiritso. Izo zikhoza kuchitidwa. Azibusa aang'ono amene anali ndi mipingo yaying'ono ya thuu ndi foro, ndi zina zotero, anakolera moto ndipo anawona masomphenya, anagwedeza Lupanga ndipo anapita, ndipo anamunyoza mdani.

⁹⁶ Inu mukudziwa bwanji kuti alipo? Alipo amuna opambana, Congressman Upshaw, King George waku England, ndi amuna opambana ambiri amene anagona odwala ndi osautsika, amachiritsidwa ndi Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse. Chotero iwo sangathe kunena kanthu za izo tsopano. Izo zachitika. Ndithudi! Iye anali . . .

⁹⁷ Kenako anapita Eliya. Pambuyo . . . Chikhumbo cha mtima wake wonse chinali kupeza lonjezo limenero. Iye ankafuna lonjezolo. Zimenezo zinali zolinga zake. Izo zinali zonse zake. Umenewo unali moyo wake. Icho chinali cholinga chake, chirichonse. Zonse, chirichonse, zinakangamira pa kupeza lonjezo limenero.

⁹⁸ Ndine wokakamizika kukhulupirira kuti sindife owona mtima pa chinthu ichi chimene tikuchikamba. Ngati cholinga chanu chonse, mmawa uno, chikukhazikika pa, “Kumpatsa Mulungu matamando chifukwa cha machiritso anga. Ndine wotsimikizika kuti ndichiritsidwa ndi Mphamvu ya Mulungu. Ndine wotsimikizika kuti ndizikhala moyo wa Chikhristu. Ndine wotsimikizika kuti ndiziyenda mu mtendere ndi Mulungu. Ndine wotsimikizika kuchita zimenezo. Ine sindikusamala zimene amayi akunena, zimene mpingo ukunena, zimene abusa akunena, zimene wina aliyense akunena, zimene dziko likunena. Ndine wotsimikizika. Ndiwo umodzi wa mtima wanga.” Inu mufika penapake ndiye.

⁹⁹ Kenako, pamene Elisha anawona kuti watsimikizika kutenga icho, Eliya anawona kuti *Elisha* watsimikizika, anamupatsa iye lonjezolo. Tsopano, lonjezo linali, “Ngati iwe udzandiwone ine ndikupita! Ngati iwe udzandiwone ine

ndikamadzachoka!” Tsopano icho chasiyidwa kwa Elisha. Iye ankafuna kuti amve lonjezo, chotero iye analandira lonjezo. Tsopano pali “ngati” mmenemo. “Ngati iwe udzandiwone ine ndikamadzapita!”

¹⁰⁰ Tsopano, ngati inu mukudwala mmawa uno, ndipo inu mukufuna kuti muchiritsidwe, ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti Khristu anakupatsani inu lonjezo. Lonjezolo ndi lanu, “Ngati inu mungakhulupirire! Ngati inu mungakhulupirire!” Musati mugonjetsedwe.

¹⁰¹ Tsopano Elisha atakulungidwa mu mkanjo wa Eliya, mneneri. Ndi kuguba bwanji kwa mgonjetsi! Momwe iye ankayendera, akupita Kumwamba, ngati mgonjetsi! Iye anali atamva lonjezo. Iye anamverera mphamvu. Iye ankayenda ngati wankhondo, mpaka ku Yordani.

¹⁰² Matamando akhale kwa Mulungu, mzanga! Wokhulupirira aliyense, mmawa uno, amene wavala chirungamo cha Khristu, akuyenda kulowera ku msewu wa Yordani. Uko nkulondola.

¹⁰³ Siyani mabomba a atomiki abwere; msiyeni iye, mwanjira iliyonseyo. Ife tavalala mwinjiro ndipo tikuyenda, mgonjetsi. Amen. Ine . . . “Musawope. Ine ndagonjetsa dziko lapansi.” Inde, bwana! Mukukumbukira chiyani? “Ine ndaligonjetsa dziko lapansi.” Khristu ananena zimenezo.

¹⁰⁴ Eliya ankayenda atavala mwinjiro wosiyiridwa, ngakhale ngati mgonjetsi, molondola, akubwera ku Yordani.

¹⁰⁵ M’bale, ndiloleni ine ndinene izi mwa ulemu kwa inu. Inu musavale mwinjiro wa wina umene wadyedwa ndi njenjete ndi kukaikira, kumene kugonjetsedwa konse uku ndi zikhulupiriro ndi zokwera-ndi-zotsika zayika mabowo mmenemo, ndipo izo zikuwukha. Inu muvale mwinjiro wa Mgonjetsi, Khristu. Musadalire mpingo wanu umene unaphunzitsapo chipulumutso mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, umene nthawi ina unkaphunzitsa machiritso Auzimu ndipo tsopano akuwukana Iwo, zonse zodyedwa ndi njenjete za kukaikira ndi china chirichonse. Muvale mwinjiro wa Iye amene sanagonjepo pa nkondo, pakuti inu muli pa njira yanu waku Yordani. Amen.

¹⁰⁶ Tsopano, iye anali atavala mwinjiro wosiyiridwa, izo nzoona. Ndipo ambiri a anthu mmawa uno avala miinjira yosiyiridwa. Koma pamene iye anadzafika ku Yordano, iye anzindikira kuti mwinjirowo pawokha sukanagwira ntchitoyo. Uko nkulondola. Ndipo mpingo, Amethodisti, Abaptisti, Achipentekoste, Apresbateria, “Oh, tiri nawo masukulu! Ku. . . Mai, ife tiri ndi zikhaliidwe zonse, za Baibulo, tazimvetsa mwangwiro. Ife tiri ndi mwinjiro wolukidwa bwino, malonjezo. Tiri nazo zonsezo. Oh, ife tinabatizidwa, tikupita kumeneko. Ndipo ndife autumwi kwambiri. Ife tavalala chikhulupiriro cha utumwi. Ife timakhulupirira mu machiritso Auzimu. Timakhulupilira

mwa Mulungu. Timakhulupirira mu Mphamvu za Mulungu. Ife tinabatizidwa, mu Baibulo, momwe Baibulo limanenera. Ife tinalandira Mzimu Woyera. Ife tinayankhula mmalirime. Ife tinachita zonsezo.” Koma, m’bale, ngati icho chiri chinthu chokhacho chimene inu mukuchisowa, inu muchipeza chosowa chanu, inunso, pamene inu mubwera ku Yordano.

¹⁰⁷ Oh, inu mukhoza kuphunzitsidwa. Inu mukhoza kukhala anzeru. Mukhoza kukhala ndi D.D., Doctor of Divinity. Inu mukhoza kukhala ndi Ph.D., Doctor of Philosophy. Mukhoza kukhala ndi LL.D., Doctor of Latin. Mukhoza kukhala ndi madigrii amitundu yonse. Inu mukhoza kukhala ndi mwinjiro wa mpingo wa Methodist pa inu. Inu mukhoza kukhala ndi mwinjiro wa mpingo wa Chipentekoste pa inu. Inu mukhoza kukhala ndi mwinjiro wa Assemblies pa inu, kapena Aumodzi, kapena Autatu, kapena chirichonse chimene chingakhale. Zimenezo ndi mwinjiro wosiyiridwa, kuyamba ndi kuyamba, uko nkulondola, za nthano zina zopangidwa ndi anthu, zoganiziridwa, zina zotero monga choncho; ndipo ngakhale ngati inu mwakhala Mkristu, ndipo mpingo wakhala Mkristu, ndi kuvala molondola.

¹⁰⁸ Koma pamene Elisha anaimirira, mowonekera, mmphepete monse mutadzaza aneneri ndi otsutsa, akuyang’ana chimene iye akanati achite, ndipo apa iye akubwera, akuyenda atavala mwinjiro wa Eliya, oh, mai, aleluya, iye waphunzitsidwa mwanjira ina, iye waphunzitsidwa, iye wagonjera, iye akukhulupirira, palibe cholakwika ndi iye, iye akubwera ku Yordano, dziko likumuyang’ana iye.

¹⁰⁹ O Mulungu, momwe ife tikuzisowera zimenezo lero! Ndi masikolala ophunzitsidwa ambiri ndi ophunzira; ndi amuna ambiri amene angathe kung’amba Baibulo ilo ndi kuliyika Ilo pamodzi, mu masamu; amuna ambiri amene angachite zinthu zazikulu mu njira za kuphunzitsa; amene amadziwa mbiriyakale ya Baibulo mpaka nthawi ino, amene angakuuzeni ora limene kandulo inayatsidwa, ndi ora limene inadzazima. Iwo akhoza kukuuzani inu zinthu zonsezi. Ndipo iwo. . .Iwo analandira ubatizo wa mmadzi. Iwo ali ndi ubatizo wauzimu, monga iwo amawutcha iwo, mwinjiro. Iwo ali nacho chirichonse chitakhala mu dongosolo.

¹¹⁰ Momwemonso Eliya anachita. Koma pamene iye anadzabwera ku Yordano, kuti adzakomane ndi dziko lotsutsa, kodi iye anafuulira chiyani? “Ali kuti Mulungu wa Eliya?” Sunali mwinjiro wa Eliya umene unachita izo. Inali Mphamvu ya Mulungu wa Eliya, imene inachita izo.

¹¹¹ Ndipo chinthu chimene dziko likuchisowa mmawa uno ndi Mphamvu ya Mulungu wa Eliya. Inu mwina munayankhulapo ndi malirime ndi kufuula, ndi kuthamangira pansi. Koma chimene ife tikuchisowa ndi Mphamvu ya Mulungu wa

Pentekoste, kupanga miyoyo ndi zinthu zimene zinali moyo mu tsiku limenero, mu mphamvu ya utumwi.

¹¹² Mwinjiro wosiyiridwa unali wabwino, koma iye ankasowekera kuyitana kwatsopano mu mtima mwake kuchokera kwa Mulungu. Iye ankasowekera kudzoza kwatsopano kuchokera kwa Mulungu. Iye anavala mwinjiro wosiyiridwa pamene iye anafika pa mtsinjepo, koma iye ankasowekera kuyitana kwatsopano kuchokera kwa Mulungu, ndi Mphamvu yatsopano yochokera kwa Mulungu, kuti ichite chozizwitsa.

¹¹³ Ndipo, m'bale wanga, inu musachite mantha kumupempha Mulungu chirichonse. Mukuyenera kumuza Mulungu, kapena kumupempha Mulungu, chirichonse chimene Iye analonjeza. Pakuti, ngati ine ndikuwonetsera Mulungu amene ali wamphamvu ndi wamphamvu zonse, ndipo ngati ine ndiri wantchito wa Mulungu, ine ndikuyenera kuchita ntchito za Mulungu. Ndipo ngati ine ndikuchita ntchito za Mulungu, ine ndikuyenera kumufunsa Mulungu kuti akwaniritse zinthu izi, chifukwa Iye akufuna kwa ine kuti ndibweretse zosathekazo. Ine ndikuyenera kumufunsa Iye. Ine ndikuyenera kuyitanira pa Iye, ndi kuyima pamenepo ndi kuti, "Mulungu, Inu munalonjeza izo." Chomwechonso inu, munthu aliyense.

¹¹⁴ "Inu mudzalandira mphamvu," Machitidwe 1:8, "Mzimu Woyera ukadzabwera pa inu." Mzimu Woyera ukadzabwera pa inu! Inu mutatha kuvekedwa ngati Mkhristu, chikhulupiriro chanu chitakhazikika mwa Khristu, ndiye inu mudzalandira mphamvu. Ndi zimenezotu pamenepo. Inde.

¹¹⁵ Ndipo, m'bale, mlongo, mmodzi aliyense wa inu, mmawa uno, mundilole ine ndinene ichi ndisanapempherere odwala, mundilole ndinene ichi: Mwa thandizo la Mulungu, mundipempherere ine. Monga ine ndinaima, zaka teni zapitazo, pa nsanja iyi, ndikulalikira za Davide ndi Goliati, tsopano si Goliati amene wanditchinga ine, koma Mulungu wamupha iye pamaso panga, koma chinthu chimene chanditchinga ine, ndi kusowa kwa chikhulupiriro, kusowa kwa chinachake chimene ine ndimadziwa kuti chinalipo.

¹¹⁶ Ndipo mmawa uno, pamaso pa kachisi wamng'ono uyu kachiwiri, ine ndikufuula: ali kuti Mulungu amene anapereka lonjezo ili? Ali kuti Mulungu amene anakomana nane ndi izi, kutsidya kuja? Bwerani patsogolo, Mulungu, ndipo dzandipatseni ine kulimbika mtima. Dzandipatseni mphamvu. Ndipatseni ine malingaliro otsimikizika, mosalabadira zimene zikubwera kapena zikupita. Kaya zikuwoneka zakuda, kapena zikuwoneka... Mulimonse mmene zikuwonekera, kazipitirirani. Lonjezolo ndi loona.

¹¹⁷ Ndipo m'bale, mlongo, limodzi la masiku awa... Kwa inu abwenzi ochimwa pano mmawa uno, ndi kwa inu anthu amene

mukuyesera kutsanzira Chikhristu, inu mukhoza kukhala a mpingo, izo ndizabwino kwambiri, ine ndiribe kanthu koti ndinene motsutsa izo, ndiribe chotsutsa maphunziro anu abwino a usikolala, kapena chotsutsa zaumulungu zanu, Ine ndiribe kanthu kotsutsa izo, koma, oh, ali kuti Mulungu?

¹¹⁸ Sanali Eliya, kuwonjezera apo. Sanali Eliya amene anatsegula mtsinje umenewo. Sunali mwinjiro wake. Elisha anawuchotsa iwo paphewa lake. Iye anawupinda iwo chimodzimodzi basi momwe Eliya ankachitira. Koma pamene iye anayamba kuyesera kuti awukupize iwo, panalibe Mphamvu pamenepe. Zitatero iye anafuula, podziwa kuti Mulungu anali penapake, “Ali kuti Mulungu ameneyo? Iye ali kuti?” Kenako chinachake chikuyenera kuti chinamukhudza mneneriyo, pakuti anawukupiza mwinjiro umenewo, ndipo akanantha madzi, ndipo iwo unatseguka kuno ndi uko. Ndipo pamaso pa azibusa a tsiku limenero, pamaso pa otsutsa a tsiku limenero, iye anayenda kuwoloka Yordano, monga momwe Eliya anachitira iye asanatero.

¹¹⁹ Ife sitikusowa ziphunzitsa; ife tiri nazo izo. Koma ife tikusowa Mulungu wa Eliya. Ife tikusowa Mphamvu ya Mulungu wa Eliya, kuti ibwerere mu mpingo wathu. Mphamvu yopangitsa icho kugwira pamenepo, ndi kutchula Mawu a Mulungu, “Olondola,” mosalabadira.

¹²⁰ Ndipo ndife, aliyense pano mmawa uno, monga anthu, pa ulendo wathu waku Yordano. “Ndipo pamene iye anafika ku Yordano.” Inu mudzafika kumeneko, umodzi wa mmawa uno kapena umodzi wa mausiku awa.

¹²¹ Pamene anadzafika ku Yordano, iye anayenda ngati mgonjetsi. Koma, pamene iye anadzafika ku Yordano, kumeneko kunali chosiyanyitsa chake. Iye anali atavala mwinjiro wosiyiridwa. Munthu wina anali atawuvala iwo. Koma iwo unali mwinjiro wabwino, ndipo iye ankadziwa chimene munthu amene anavala mwinjirowo anali.

¹²² M'bale, mlongo, umodzi wa mmawa uwu, ine ndikuyenera ndidzafike uko ku Yordano.

¹²³ Ndimaganiza. Masana ano, ife tikupita uko kwa M'bale ndi Mlongo Wright. Musawayiwale iwo. Ichi ndi chikumbutso chawo chaukwati cha zaka fifite. Ine ndikukhulupirira, mpingo, iwo akakhala ndi—chakudya chamadzulo ndi iwo. Ine ndimaganiza, tsiku lina: zaka fifite! Ndipo ine ndikuwawona iwo awiri onse, okalamba ndi okanthidwira pansu. Ine ndinaganiza, “Inde, ndiri ndi zaka forte-seveni zakubadwa.” Iwo anali atangokwatirana kumene zaka zitatu ine ndisanabadwe.

¹²⁴ Forte-seveni! Ine ndikuyenda kupita chaku Yordano. Ndikuyenera kutsikira kumusiko. Ndikuyenera ndikafike kumeneko. Ine ndidzakafika kumeneko. Zikhoza kudzakhala mu ngozi pa msewu. Ine ndikhoza kudzagwa kuchokera mu

mlengalenga, mu ndege. Ine ndikhoza kuwomberedwa, ndi muvi wa mdierekezi kwinakwake, ndi kufa. Sindikudziwa momwe ndidzapitire. Koma, pali chinthu chimodzi chimene ndikuchidziwa, ine ndikupita, ndipo ine ndikuyenda kumapita ku Yordano.

¹²⁵ Koma pamene ndidzafika kumeneko, ine ndikufuna ndidzadziwe chinthu chimodzi, kuti ine ndavala mwinjiro wosiyiridwa, inenso. Ine sindikudalira mu wanga, chifukwa iwo siwabwino. Pakuti, Eliya atangonyamula mwinjiro wa Elisha, anawung'amba wake mzydutsa ndipo anawuponyera iwo pansi. Ndipo umu ndi momwe zinaliri pamene ine ndinamupeza Khristu. Ine ndinadzing'amba ndekha, malingaliro anga omwe, zamkutu zanga zomwe, kanthu kanga kakang'ono. Ine ndinaganiza, pamene ine ndinali wamng'ono, mlaliki wa Baptisti, ine ndinali basi pafupifupi. . . Ine ndinali winawake. Koma, ine ndinawung'amba iwo; ndinavala mwinjiro Wake. Ndipo pamene ine ndidzafika ku Yordano, ine ndikufuna ndidzadzipeze ndekha nditakulungidwa mu mwinjiro Wake. Iye adzatsatira zimenezo. Ndipo tidzakafika kumeneko tsiku lina.

Koma tiyeni tipemphere mphindi chabe.

¹²⁶ Atate Akumwamba, pamene ife tiri pa kuyenda kwathu kwaku Yordano mmawa uno, monga agonjetsi, ndipo tsiku lina, ife tikuyenera tidzapereke chinachake ku Yordano, ndicho, ku imfa. Ndipo, oh, chidzakhala chinthu choyipa bwanji chimenecho, kulekanitsidwa kwa Mulungu. Sitidzatha kuwoloka. Ayi. Koma, Eliya, pamene iye anafika kumeneko, iye anali atavala mwinjiro wa Elisha. . . mwinjiro wa Eliya. Ndipo pamene iye anavula mwinjirowo. . . wa Eliya, munthu amene anali wokondweretsa-bwino pamaso Panu, ndipo Inu munali mutamulandira iye ndipo munamubweretsa iye Kumwamba ndi Inu. Ndipo Elisha anali atavala mwinjiro wake, chotero iye anapereka ku Yordano, imfa, mwinjiro wa Eliya. Ndipo iwo unalandiridwa, ndipo Yordano anatseguka, ndipo iye anawoloka.

¹²⁷ Wokonedwa Mulungu, tsiku lina, ife tikuyenera kuti tidzabwere kumeneko. Ife sitingathe kupereka ntchito zathu zabwino; ife tiribe. Ife sitingathe kupereka chirichonse padziko lapansi. Ine sindikukhumba ngakhale chirichonse, kuyesera kupereka, koma ndikudalira kwathunthu muzoyenera za Yesu. Inu munamulandira Iye, ndipo munamuukitsa Iye kwa akufa, ndipo Iye anabweretsedwa pamaso pa Mulungu ndipo kumeneko adzakakhala kwanthawizonse. Ndipo, Mulungu, ine ndikufuna kupereka izo kwa Inu, kuti ine ndimakhulupirira pa Iye, ndipo ine ndimamukonda Iye. Ndipo, mwa chisomo Chake, Iye wativeka ife ndi mwinjiro Wake. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mutithandize ife tsopano mmasiku a nkondo. Ndi kumene anthu a Mulungu akuyenera kuchita ntchito za

Mulungu, ndikupemphera kuti Inu mutilole ife titenge mwinjiro wa Khristu, mphamvu ya Mzimu Woyera, ndi kuyitanira Mulungu amene anakhala mwa Iye. Perekani izi. Mu Dzina la Khristu ife tikupempha izi.

¹²⁸ Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ine ndikungodabwa, pano mmawa uno, ngati alipo munthu amene akuyesetsa kuti ayende kupita ku Yordano, asanavale mwinjiro uwu. Ngati alipo munthu amene sanavale mwinjiro wa Yesu Khristu pa inu, ndipo ngakhale iwo unavalidwa nthawi ina ndi Mwana wa Mulungu. Ine ndikudabwa, ngati inu simunavale iwo mmawa uno, ngati inu mungakweze manja anu kwa Mulungu ndi kuti, “Wokonedwa Mulungu, ora lino, ine tsopano ndikufuna kuti ndivomereze izo.”

¹²⁹ Mulungu akudalitse iwe, dona. Kodi winawakenso, mungakweze dzanja lanu? Mulungu akudalitse iwe, mwana. Winawakenso, mungakweze mmwamba dzanja lanu? Mulungu akudalitse iwe, mnyamata wamng’ono. Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Winawakenso angakweze dzanja lake? Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo uko, bwana.


¹³⁰ Mungonena izo, “Mwa thandizo la Mulungu, mmawa uno, ine ndikufuna kusiya kudzilungamitsa kwanga, malingaliro anga omwe, ndi malingaliro anga a zosangalatsa ndi nthawi yayikulu, ndi tchimo limene ndakhalamo. Ndipo ine ndikufuna Khristu kuti ayike mwinjiro Wake pa ine, mmawa uno, kuti ine ndigwiritse ntchito mwinjiro Wake. Ndikudziwa kuti ndi Iwo ndi wangwiro.” Mulungu akudalitse iwe, mwana. Winawakenso akuti, “Ndipo ndingokweza . . .”

¹³¹ Inu kwezani dzanja lanu, munene, “Ine tsopano ndikufuna kuvomereza Mzimu Woyera mmoyo wanga. Ine ndikufuna kuti ndivekedwe mu chirungamo Chake. Ndikadzafika kumeneko tsiku limenero, sindidzadzzipereka ndekha ndikuti, ‘Chabwino, tsopano, Inu mukudziwa ine ndinamugulira winawake makala. Ndinachita ichi.’” Zimenezo ndi zabwino, ndi zabwino kwambiri, koma izo. . . Chinachake chimayenera kufa, kuti inu mudzakhale moyo, ndipo kokha kudzera mu kuchita kwa zimenezo inu mukhoza kupulumutsidwa. Kodi inu mungakweze dzanja lanu? Ndikuti, “Khristu, ine tsopano ndikusiya njira yanga yomwe. Ine ndikuvomereza njira Yanu. Ine ndikufuna Inu mundichitire ine chifundo pamene ine ndidzafike pa mathero a msewu?” Chabwino. Mulungu akudalitse iwe, dona. Mulungu akudalitse iwe. Chabwino.

Tsopano ife tikhala ndi pemphero.

¹³² Tsopano, Atate Olungama, Akumwamba, ena seveni, eyiti, manja teni akwezedwa mmwamba. Sindikudziwa momwe iwo aliri. Inu mukudziwa zonse za iwo. Ine sindikudziwa. Koma iwo akusowa lero. Ndipo iwo azindikira kuti iwo akusowa, ndipo iwo akulolera kuti abwere ndi kudzalandira thandizo mu nthawi ya

vuto; kudzawona kuti, ora lalikulu limene layandikira tsopano, mabomba a atomiki, zinthu zazikulu zimene zikutiyembekezera ife.

¹³³ Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu muwadalitse anthu awa, ndipo lero ikani dzanja Lanu pa iwo ndi kuchotsa mphulupulu zawo zonse ndi kukaikira. Ndipo mulole iwo ataye mwinjiro wawo wakale wodyedwa ndi njenjete wa kudzilungamitsa kwawo, kumene chimbalanga ndi nkholulu, ndi njenjete za zauzimu ndi zachitchalitchi, zabowola mabowo mwa izo, ndipo (iwo) siwukhalitsa panonso. Mulole iwo angotayira iwo kutali, ndi kufikirako ndi kukatenga mwinjiro wa Ambuye Yesu. Nkumati, “Ine ndikudalira mwa Iye. Ndikudzikulunga ndekha, osati mu chirungamo changa, kapena maganizo anga omwe. Koma, kuyambira ora lino mpakana, ine ndikudalira Inu.” Perekani kuti iwo alandire izo, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Amenii. 

56-1125M Mwinjiro Wosiyiridwa
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org